# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NYENGO MSABATAYI


## KUYAMBIRA PA 15 MPAKA PA 21 DECEMBER, 2025

### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Nyengo ya mitambo ndi yotentha komanso ya mvula ikuyembekezereka kupitilira m'madera ambiri. Mvulayi ikuyembekezereka ku**gwa yamphamvu m'madera ena maka a m'phepete mwa nyanja ya Malawi.** Izi ndi kamba ka mphepo zosakhazikika zomwe zikuyembekezereka**.**

**Mphepo zikuyembekezereka kuomba mwamphamvu nthawi zina pa nyanja zathu.**

*Mapu oyambilira omwe ali Kumanja akuonetsa kuchuluka kwa mlingo wa mvula yomwe ikuyembekezereka m'sabata ikudzayi.*





*Ulosi wamvula musabata ikudzayi. Kuphatikiza masiku onse musabatayi.*

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo ya mphepo, yamitambo ndi yotentha komanso mvula yamabingu yomwe m'madera ena inagwa yamphamvu**.** Mlingo wa mvula yambiri omwe tinalandira unachokera ku Dwangwa boma la Nkhotakota ndi mlingo wa **88mm** pa **10 December 2025.**

*Mapu ali kumanja akuonetsa mlingo wa mvula yochuluka yomwe inagwa m'sabata yangothayi.*




*Mapu akuonetsa kuchuluka kwa mlingo wa mvula m'sabata yangothayi*

### MALANGIZO M'SABATALI

- **Tipewe kuoloka madzi omwe asefukira kapena omwe akuthamanga kwambiri**.
- **Mvula yamabingu:** Tikhale m'malo otetezeka
- **Pa nyanja:** Asodzi akupemphedwa kupewa kulowa pa nyanja mphepo ya mphamvu ikamaomba.

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO**

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 14 December, 2025**